

AKHRISTU KUTHANDIZA
AKHRISTU ENA KUKULA

AKHRISTU KUTHANDIZA AKHRISTU ENA KUKULA

lolembedwa ndi
Gena Hampton

chithunzithunzi ndi
Pamela Swafford

AKHRISTU KUTHANDIZA AKHRISTU ENA KUKULA

Maphunziro Akuphunzitsa

Mmene Tingakhalire Ophunzira Enieni

CHOYAMBA:

1. Cholinga cha Akhristu Kuthandiza Akhristu Ena Kukula ndi kukuphunzitsani kuti mukhale ofanana ndi Yesu kuposa mmene mulili tsopano. Mudzaphunzitsidwanso mmene mungathandizire ena kuti akhalenso a Khristu, ndipo mudzawaphunzitsanso iwo kukula monga a Khristu.
2. Gulu lathu lidzakhala la mamembara a anthu okwana awiri mpaka kapena asanu ndi mmodzi amene adzakhala ali kukumana pamodzi kuphunzira ndi kugawana pa Sabata.
3. Sabata iliyonse tidzakhala tili kuloweza malemba, kuphunzira Bukhu Lopatulika, kupemphera pamodzi ndi kuphunzira mmene tingachitire umboni.

I. MAPHUNZIRO:

A. Malembo Oloweza pa Mtima

1. Mudzaphunzira malembo m'ndime ziwiri Sabata iliyonse. Izi zidzayikidwa pa m'ndandanda wa makonzedwe a maphunziro anu.
2. Mtsogoleri wanu adzaonetsetsa ngati ndimezi mwaziphunziradi - pa Sabata.
3. Muyenera kubwereza ndime iliyonse imene muphunzira pa tsiku kwa miyezi iwiri.

B. Phunziro la M'Bukhu Lopatulika

1. Sabata iliyonse mtsogoleri wanu adzatsogolera maphunziro a Bukhu Lopatulika. Malembo ofunika a Mawu a Mulungu ali pa pepala la maphunziro ena.
2. Muyenera kuphunzira malembo ofunikawo kunyumba kwanu tsiku ndi tsiku. Potsiriza yankhani mafunso amene ali kotsirizira kwa phunziro lanu.
3. Kukadakhala kwabwino ngati mutayamba. Kuwerenga Bukhu la Uthenga wabwino wa Yohane tsiku ndi tsiku pa nthawi yanu ndi Mulungu.

C. Pemphero

1. Mtsogoleri wanu adzakhala akutsogolera mapemphero a Sabata ndi Sabata.
2. Muyenera kusankha nthawi yopemphera tsiku ndi tsiku.
3. Kumbuyo kwa phunziro lanu mudzapezako malo amene mudzakhoza kulembapo zoyenera kupempherera. Mtsogoleri wanu adzakuthandizani kukonza m'ndandanda wa zoyenera kupempherera.

D. Kuchitira Umboni

1. Ndime zimene mukuphunzira m'Bukhu Lopatulika si zainu nokha ayi. Muyenera kugawana nawo anzanu ndimezi.
2. Mtsogoleri wanu adzakuphunzitsani mmene mungamayendere pochezera anthu, ndi kuwachitira umboni.
3. Mudzaphunzira kujambula Ulalo wa Moyo ndi Dzanja ndiponso Kujambula Mtanda wa Moyo. Zithunzizi zidzakuthandizani pamene muli kuchitira umboni.

II. MAWUMBONI:

Pofuna kuthandizana wina ndi mzake kuti tidziwane bwinobwino, aliyense wa ife ayenera kupereka umboni wake mwachidule.

- A. Tiuzeni amene anakuthandizani kwambiri m'moyo wanu wa chiKhristu.
- B. Tiuzeni mmene munthuyu anakuthandizirani.

POMALIZA:

1. Udindo wanu woyamba ndi kuwerenga malembo ndi kuphunzira maphunziro oyamba.
2. Nonse pamodzi mogwirizana, konzani malo ndi nthawi ya misonkhano yanu kapena kukumana kwanu.
3. Potsiriza pa misonkhano yanu, muyenera kupemphera.

PHUNZIRO 1

Kuloweza Mawu Apamtima: Aroma 3:23, Aroma 6:23

Kuphunzira Bukhu
Lopatulika:

Chitsimikizo Cha
Chipulumutso

Yohane 5:24

Amene amamva mawu anga ndi
kukhulupirira Iye amene
anandituma Ine, ali ndi

Yohane 10:27-28

Kodi ndani amene angathe
kulanda nkhoa za Yesu
kuchokera kwa Iye?

Aroma 8:16

Mzimu wa Mulungu akuti
ndife

Aroma 8:35-39

Kodi nchiyani chimene
chingatilekanitso ndi
chikondi cha Khristu?

Pemphero:

Kambiranani za m'ndandanda
wa mapemphero. Pempherani
pamodzi.

Umboni:

Mtsogoleri aphunzitse
chigawo chimodzi cha Ulalo
wa Moyo.

PHUNZIRO 2

Kuloweza Mawu Apamtima: Ahebri 9:27, Aroma 5:8

Nenani Mawu apamtima amene munaphunzira Sabata yatha.

Kuphunzira Bukhu

Lopatulika:

Masalmo 5:3

Nthawi Ya Padera

Kodi amene analemba Masalmo analikupemphera nthawi yanji?

Marko 1:35

Kodi Yesu anapemphera nthawi yanji ndiponso kuti?

Luka 10:39

Kodi Maria anasankha kuchita chiyani?

Luka 11:9-10

Kodi Yesu akukuuzani kuti muchite chiyani?

Pemphero:

Ikani mayina a bwenzi ndi abale amene ali otayika pa m'ndandanda wa mapemphero anu. Pempherani pamodzi.

Umboni:

Mtsogoleri aphunzitse chigawo chomaliza cha Ulalo wa Moyo.

PHUNZIRO 3

Kuloweza Mawu Apamtima: Aefeso 2:8-9, Yohane 5:24

Nenani Mawu apamtima a phunziro 1 ndi 2.

Kuphunzira Bukhu
Lopatulika:

Ahebri 13:15

1 Yohane 1:9

Aefeso 5:20

Afilipi 4:6

Pemphero

Kodi tipereke chiyani kwa Mulungu?

Kodi timalandira bwanji chikhululukiro cha zoyipa zathu?

Kodi ndi zinthu ziti zimene tiyenera kuthokozera Mulungu?

Ndikafuna chinthu, ndiyenera kutani?

Pemphero:

Kambiranani za nthawi yanu imene muyenera kukhala chete. Konzani dongosolo la kawerengedwe ka Uthenga wa Yohane.

Pempherani pamodzi chifukwa cha abwenzi amene ali otayika.

Umboni:

Mtsogoleri aphunzitse zigawo zonse za Ulalo wa Moyo. Sabata ya mawa mudzaphunzitse mtsogoleri wanu kapena kuphunzitsana ndi arzanu.

PHUNZIRO 4

Kuloweza Mawu Apamtima: Chibvumbulutso 3:20,
Yohane 5:11-12

Kuphunzira Bukhu
Lopatulika:

Umbuye wa Khristu

Afilipi 2:9-11

Onse adzanena kuti Yesu
Khristu ndi

Luka 9:23

Yesu anati tiyenera kusenza
_____ wathu

masiku onse ndi kumu-_____

Luka 6:46-47

Otsatira Yesu ayenera kumva
mawu ake ndi kuwa-
_____ ntchito.

Pemphero:

Pempherani chiwalo
chilichonse cha (membala)
gulu lanu.

Umboni:

Mtsogoleri wanu aphunzitse
chiwalo chilichonse cha
gulu lanu za Ulalo wa Moyo.

Musanakumane pa msonkhano
wanu wotsatira phunzitsani
munthu wina za Ulalo wa
Moyo.

PHUNZIRO 5

Kuloweza Mawu Apamtima:	Bwerezani kunena ndine zonse za Ulalo wa Moyo.
Kuphunzira Bukhu Lopatulika:	<u>Mawu</u>
Aroma 10:17	Chikhulupiriro chimachokera kwa
Chibvumbulutso 1:3	Odala ndi amene
Masalmo 119:11	Ndidzasunga lamulo lanu
Masalmo 119:97	Tsiku lonse ndidza lamulo lanu.
Machitidwe 17:11	Tsiku lili lonse ndiyenera
Yakobo 1:22	Mawu apamtima. Ndidzayika mawu ake mu
Pemphero:	Mukatha kuwerenga Uthenga wa Yohane pa nthawi yanu yokhala chete, muyambe kuwerenga Uthenga wina kuchokera m'Bukhu Lopatulika. Sankhani wopemphera naye ndipo muzipemphera pamodzi sabata ili yonse.
Umboni:	Phunzitsani za Ulalo wa Moyo kwa anthu awiri sabata ino. Pemphani chithandizo kuchokera kwa mtsogoleri wanu ngati mungachifune.

PHUNZIRO 6

Kuloweza Mawu Apamtima: Aroma 10:17, Masalmo 119:97

Kuphunzira Bukhu
Lopatulika:

Mpingo Ndi Inu

Akolose 1:18

Yesu ndi mutu wa Thupi lake

Machitidwe 2:41-42

Kodi ndi zinthu ziti zimene
ziwalo za mpingo zinachita?

Akolose 1:28-29

Mpingo uyenera kulalikira
za Yesu kwa anthu ati?

Pemphero:

Kambiranani zimene
mwatsiriza mu nthawi
yokhala chete. Pempherani
mbusa wa mpingo wanu.

Onjezerani mayina a anthu
amene ali otayika pa
m'ndandanda wanu wa
mapemphero.

Umboni:

Mugwiritse ntchito Dzanja
kusonyeza mmene
tingakhalire m'Mawu a
Mulungu.

Mtsogoleri wanu
adzakuthandizani ndi Mawu
a pamtima.

Kambiranani mavuto amene
mwawapeza pakuphunzitsa
Ulalo wa Moyo.

Bweretsani bwenzi lanu ku
mpingo sabata ya mawa.

PHUNZIRO 7

Kuloweza Mawu Apamtima: Chibvumbulutso 1:3,
Machitidwe 17:11

Kuphunzira Bukhu
Lopatulika:

Chiyanjano

Ahebri 10:24-25

Ndi khalidwe la bwino ku

Machitidwe 2:43-47

Okhulupirira anagawana
zinthu zawo ndi

Mateyu 18:20

Okhulupirira akasonkhana
pamodzi Yesu ali

Yohane 13:34-35

Yesu akutilamulira kuti ti-

Pemphero:

Pempherani chiyanjano cha
okhulupirira mumpingo
mwanu.

Umboni:

Gwiritsani ntchito Dzanja
kusonyeza mmene
tingakhalire m'Mawu a
Mulungu.

Chezani ndi wina amene
akusowa chiyanjano cha
Chikhristu.

PHUNZIRO 8

Kuloweza Mawu Apamtima: Masalmo 119:11, Yakobo 1:22

Kuphunzira Bukhu
Lopatulika:

Luka 6:38

2 Akorinto 8:1-5

2 Akorinto 9:6-8

Miyambo 3:9-10

Pemphero:

Umboni:

Udindo Wa Chikhristu

Patsani kwa anzanu ndipo
Mulungu adza-

Mipingo inali ya chifundo
m'kupereka kwawo ngakhale
inali

Mulungu amakonda amene
amapereka

Lemekezani Mulungu ndi

Pempherani za kupereka
chakhumi cha chuma chanu
kwa Mulungu.

Sabata ino gwiritsani
ntchito Dzanja lanu
kusonyeza anthu awiri mmene
tingakhaliye m'Mawu a
Mulungu.

Lembani lonjezo lanu lanu
ndi kulibweretsa ku Kalasi.

1. Moyo wanga
ndisanalandire Yesu
Khristu.
2. Mmene ndinadziwira kuti
Mulungu anali
kulankhula kwa ine.
3. Mmene ndinakhaliya
M'Khristu.
4. Zimene Chikhristu
chimatanthauza kwa ine.

PHUNZIRO 9

- Kuloweza Mawu Apamtima: Luka 14:27,
Agalatiya 2:19-20
Bwerezani Mawu apamtima
onse a m'Dzanja.
- Kuphunzira Bukhu
Lopatulika:
Yohane 14:25-26
Machitidwe 1:8
- Agalatiya 5:22-26
- Pemphero:
- Umboni:
- Mzimu Woyera M'Moyo Wanu
Mz-
adzakuphunzitsani zonse.
Mzimu Woyera amakupatsani
mphamvu zochitira umboni
kuti?
-
- Kodi Mzimu Woyera amapanga
chiyani m'miyoyo mwathu?
-
- Pempherani ndi mzanu
wopemphera naye sabata lili
lonse.
Ino ndi nthawi yanu
yotsogolera gulu kuphunzira
za Akhristu kuthandiza
Akhristu ena kukula.
Pemphani Mulungu kuti
akutsogolereni posankha
anthu awiri mpaka asanu ndi
mmodzi kukhala m'gululi.
- Perekani umboni wanu ku
kalasi yanu.
Litengereni bwenzi lanu
lotayika ku mpingo sabata
ya mawa.

PHUNZIRO 10

Kuloweza Mawu Apamtima: Yohane 8:31, Yohane 15:7

Bwerezani Malembo oyera
onse a mu Ulalo wa Moyo.

Kuphunzira Bukhu
Lopatulika:

Aefeso 4:7

Mphatso Za Mzimu Woyera

Ali yense mwa ife analandira
mphato yofunika kuchokera ku

Aefeso 4:11-12

Khristu anapereka mphatso
kwa anthu kuti amange

1 Petro 4:10

Tiyenera kugwiritsa ntchito
mphatso yathu pothandiza

Aroma 12:6-8

Lembani mphatso zisanu ndi
ziwiri zimene zatchulidwa
m'ndime zimenezi

Pemphero:

Pemphani Mulungu kuti
akuthandizeni kudziwa
mphatso yanu kupyolera mwa
Mzimu.

Pemphani utsogoleri wa
Mulungu pamene muyamba
kuphunzitsa Akhristu
Kuthandiza Akhristu Ena
Kukula Sabata ya mawa.

Umboni:

Pempherani munthu aliyense
amene adzakhale nanu
m'kalasi mwanu.
Jambulani ndikufotokoza
Mtima, Mutu ndi Mapazi a
Mtanda wa Moyo.
Perekani umboni wanu kwa
bwenzi lotayika sabata ino.

PHUNZIRO 11

Kuloweza Mawu Apamtima: Yohane 13:35, Yohane 15:8

Kuphunzira Bukhu
Lopatulika:

Aefeso 6:10-13

Aefeso 6:14-18

Ahebri 2:18

1 Akorinto 10:13

Pemphero:

Umboni:

Kugonjetsa Mayesero

Mukhoza kugonjetsa Satana
povala

Timavala za nkhondo za
Mulungu po

kupempha thandizo la
Mulungu.

Yesu angathe kuthandiza
munthu amene akuyesedwa
chifukwa Iye mwini ana

sadzalola inu
kuyesedwa koposa mmene
mphamvu zanu zingathere
kupirira.

Pempherani mphamvu
zogonjetsa mayesero anu.

Pemphani Mulungu kuti
adalitse kalasi latsopano
limene mudzayamba
kuphunzitsa sabata ino.

Mupempheni kuti
akuthandizeni kuti mukhale
okhulupirika.

Jambulani ndi kufotokoza za
Mikono ya Mtanda wa Moyo.

Phunzitsani Phunziro 1 la
Akhristu Kuthandiza Akhristu
Ena Kukula ku kalasi lanu
latsopano.

PHUNZIRO 12

Kuloweza Mawu Apamtima: Bwerezani kunena Mawu onse
a Mtanda wa Moyo.

Kuphunzira Bukhu
Lopatulika:

Yeremiya 29:11

Chifuniro Cha Mulungu
Pa Moyo Wanu

Mulungu yekha ndi amene
amadziwa za

zimene akusungirani.

Aroma 12:1-2

Lolani Mulungu kuti
atembenuze maganizo anu.
Ndipo mudzatha kudziwa

1 Atesalonika 5:16-18 Mukhale

Pempherani pa

Mukhale

m'nthawi zonse.

Pemphero:

Pemphani Mulungu kuti
akuthandizeni kudziwa ndi
kutsatira chifuniro chake
m'moyo wanu.

Pempherani mwayi wogawana
ndi anzanu: Ulalo wa Moyo,
Dzanja, ndi Mtanda wa Moyo.

Umboni:

Jambulani ndi kufotokoza
za Mtanda wa Moyo.

Pitirizani ndi kalasi lanu
latsopano.


M'NDANDANDA WANGA WA MAPEMPHERO

Tsiku

Pemphe Langa

Yankho la Mulungu

ULALO WA MOYO



1. Bukhu Lopatulika limatiphunzitsa kuti Mulungu amakonda anthu onse ndipo amafuna kuti amudziwe (Jambulani MUNTHU ndi MULUNGU ndi dzenje lakuya pakati pawo. Lembani MUNTHU kumanzere ndi MULUNGU kumanja ndi TCHIMO litawalekanitsa. Tsono lembani Aroma 3:23.)

Koma munthu analekanitsidwa ndi Mulungu chifukwa anachimwira Mulungu.

Aroma 3:23 akuti, "Pakuti onse anachimwa, naperewera pa ulemmerero wa Mulungu."

2. Zotsatira za TCHIMO limeneli ndi IMFA.

Aroma 6:23 akuti, "Pakuti mphotho yake ya uchimo ndi IMFA; koma mphatso yaulere ya Mulungu ndiyo moyo wosatha wa mwa Khristu Yesu Ambuye wathu."

(Lembani Aroma 6:23.)

3. Ife sitifuna kuti tikafa tizengedwe mlandu.
Koma. . .

Ahebri 9:27 akuti, "Ndipo popeza kwaikikatu kwa anthu kufa kamodzi, ndipo atafa, chiweruziro."

(Lembani Ahebri 9:27. Jambulani mnzere ndikulemba IMFA YOSATHA.)

4. Pali yankho. YESU KHRISTU, amene anafa pa mtanda chifukwa cha machimo athu, ndiyo njira yopita kwa Mulungu.

Aroma 5:8 akuti, "Koma Mulungu atsimikiza kwa ife chikondi chake cha mwini yekha mmenemo, kuti pokhala ife chikhalire ochimwa, Khristu adatifera ife."

Khristu, panjira ya mtanda, anamanga ulalo pakati pa MUNTHU ndi MULUNGU.

(Lembani Aroma 5:8. Jambulani mtanda kulumikiza MUNTHU ndi MULUNGU ndipo lembani KHRISTU pamtandapo.)

5. Chipulumutso ndi mphatso ya ulere ya Mulungu.

Aefeso 2:8-9 akuti, "Pakuti muli opulumutsidwa ndi chisomo chakuchita mwa chikhulupiriro, ndipo ichi chosachokera kwa inu; chili mphatso ya Mulungu; chosachokera kuntchito, kuti asadzitamandire munthu aliyense."

(Lembani Aefeso 2:8-9.)

6. Mulungu ali ndi chitsimikizo choposa kwa munthu aliyense amene adzamva ndi kukhulupilira.

Yohane 5:24 akuti, "Indetu, indetu, ndinena kwa inu, kuti iye wakumva mawu anga, ndi kukhulupirira Iye amene anandituma Ine, ali nawo moyo wosatha, ndipo salowa m'kuweruza, koma wachokera kuimfa, nalowa m'moyo."

(Lembani Yohane 5:24.)

7. Koma kuti tipeze chitsimikizo cha Mulungu, munthu ayenera kufuna kupulumutsidwa ndiponso ayenera "kutsegula khomo la mtima wake."

Chibvumbulutso 3:20 akuti, "Taona, ndaima pakhomo, ndigogoda; wina akamva mawu anga nakatsegula pakhomo, ndidzalowa kwa iye, ndipo ndidzadya naye, ndi iye ndi Ine."

(Lembani Chibvumbulutso 3:20 ndi kujambula mzere pansi pake. Lembani MOYO WOSATHA.)

8. MAFUNSO AMENE MUNGAFUNSE:

- a. Kodi mudatsegula khomo la mtima wanu kwa Yesu?
- b. Kodi pali chifukwa chokulepheretsani kumulandira Iye lero?

9. PEMPHERO LOLANDIRA YESU:

"Ambuye Yesu, lowani m'moyo wanga ndi kukhala Mpulumutsi ndi Ambuye wanga. Mundikhululukire zoyipa zanga, ndi kundipatsa moyo wosatha."

10. Ndikayitana Yesu Khristu m'moyo wanga, ndili ndi moyo wosatha. Ndidziwa izi chifukwa:

1 Yohane 5:11-12 akuti, "Ndipo uwu ndi umboniwo, kuti Mulungu anatipatsa ife moyo wosatha, ndipo moyo umene uli mwa Mwana wake."

(Lembani 1 Yohane 5:11-12 pansi pa mtanda.)

DZANJA

Ganizirani 5.
Masalmo 119:97

Lwezani 4.
Masalmo 119:11

Phunzirani 3.
Machitidwe 17:11

Chitani
Yakobo 1:22

Werengani 2.
Chibvumbulutso 1:3

Imvani 1.
Aroma 10:17

Kuti tikhale ndi Mulungu m'miyoyo yathu tiyenera kukhala ndi mawu ake m'mitima mwathu. Dzanja lisonyeza mmene tingakhalire m'Mawu a Mulungu.

1. Chala choyamba chikuyimira njira yoyamba imene tilandilira mawu pa kumva.

Aroma 10:17 akuti, "Chomwecho chikhulupiriro chidza ndi mbiri, ndi mbiri idza mwa mawu a Khristu."

2. Chala chachikulu, chachisanu chimayimira njira imene tiyenera kuganizira mawu.

Masalmo 119:97 akuti, "Ha! Ndikondadi chilamulo chanu; Ndilingiriramo ine tsiku lonse."

Ndikagwira Bukhu Lopatulika ndi chala changa choyamba ndi chachisanu, ndidzamba mawu a Mulungu, koma sindidzatha kuwagwira kwambiri. (Uzani munthu wina kuti akulandeni Bukhu Lopatulika, inu mutaligwira ndi chala chanu choyamba ndi chachisanu.)

3. Chala chachiwiri chikuyimira njira ina imene tingapezere mawu a Mulungu muntima mwathu. Iwerengeni.

Chibvumbulutso 1:3 akuti, "Wodala iye amene awerenga, ndi iwo amene akumva mawu a chinenerocho, nasunga zolembedwa momwemo; pakuti nthawi yayandikira."

Kagwiridwe kanga ka Bukhu Lopatulika, si kamphamvu kwenikweni. (Uzani munthu wina kuti achotse Bukhu Lopatulika mmanja mwanu mutaligwira ndi zala zanu ziwiri ndi chachisanu.)

4. Chala chachitatu chimayimira njira ina yakuya yotidziwitsa mawu. Phunzirani.

Machitidwe 17:11 akuti, "Amenewa anali mfulu koposa a m'Tesalonika, popeza analandira mawu ndi kufunitsa kwa mtima wonse, nasanthula m'malembo masiku onse, ngati zinthu zinali zotero."

Ndikamva, ndikaganiza, ndikawerenga, ndikuphunzira mawu ndi kovuta kuti munthu wina alande Bukhu Lopatulika m'manja mwanga. (Lolani munthu wina kuti alilande movutikira.)

5. Chala chachinayi chimayimira njira yoposa zonse yoti tipeze mawu muntima mwathu. Ilowezeni.

Masalmo 119:11 akuti, "Ndinawabisa mawu anu muntima mwanga, Kuti ndisalakwire Inu."

Poloweza mawu, amakhaladi mwa ife ndipo ifenso timakhala mwa iwo. Tsopano ndagwira mawu ndi mphamvu ndipo palibe munthu amene angandilande. (Gwirani Bukhu Lopatulika kumbuyo kwake ndipo muloleni wina kuti ayese kukulandani. Koma mulikoke ndi kulichotsa m'manja mwake.)

6. Ndinagwira Bukhu Lopatulika ndi mphamvu m'manja mwanga. Izi zimayimira kugwiritsa ntchito mawu m'miyoyo yathu.

Yakobo 1:22 akuti, "Khalani akuchita mawu, osati akumva okha, ndi kudziyenga nokha."

Ndi chinthu chofunika kuyika mawu m'mitima yathu, koma sitingakhale m'mawu pokhapokha titawagwiritsa ntchito m'miyoyo yathu.

MTANDA WA MOYO
Luka 14:27

KUTAMANDA

Pemphero
Yohane
15:7

UMBONI
Yohane 15:8

KHRISTU
Agalatiya
2:19-20

CHIYANJANO
Yohane 13:35

ULALIKI

KUTHANDIZA



KUPHUNZITSA

1. Wophunzira wa Yesu ndi amene amalola Yesu kuti akhale Ambuye wa moyo wake.

Luka 14:27 akuti, "Ndipo amene ali yense sasenza mtanda wake wa mwini yekha, ndi kudza pambuyo panga, sakhoza kukhala wophunzira wanga."

(Lembani MTANDA WA MOYO pamwamba pa pepala.
Pansi mulembe Luka 14:27.)

2. Umoyo wa Chikhristu, ndiwo kulola Khristu kukhala mwa inu.

Agalatiya 2:19-20 akuti, "Pakuti ine mwa lamulo - ndafa ku lamulo, kuti ndikhale ndi moyo kwa Mulungu. Ndinapachikidwa ndi Khristu; koma ndili ndi moyo; wosatinso ine ayi, koma Khristu ali ndi moyo mwa ine; koma moyo umene ndili nawo tsopano m'thupi, ndili nawo m'chikhulupiriro cha Mwana wa Mulungu, amene anandikonda, nadzipereka yekha chifukwa cha ine."

(Jambulani chithunzi chanu. Mutambasule mikono ngati mtanda. Jambulani mtima wanu ndi kulemba Khristu mkati mwa mtimawo ndi Agalatiya 2:19-20.)

3. Pali zinthu zinayi zimene mKhristu ayenera kuchita ngati afuna kusenza mtanda wake ndi kutumikira anzake.

- 1) Choyamba ndi KUKHALA M'MAWU A MULUNGU.
(Jambulani Mawu a Mulungu kuti inu muyimepo ndi ulemba Yohane 8:31.)

Yohane 8:31 akuti, "Chifukwa chache Yesu ananena kwa Ayuda aja adakhulupirira Iye, Ngati mukhala inu m'mawu anga, muli akuphunzira anga ndithu."

- 2) Chachiwiri ndi KUPEMPERA MWA CHIKHULUPIRIRO.
(Lembani PEMPERO mkati mwa mutu wanu ndi Yohane 15:7.)

Yohane 15:7 akuti, "Ngati mukhala mwa Ine, ndi mawu anga akhala mwa inu, pemphani chimene chilichonse muchifuna ndipo chidzachitika kwa inu."

- 3) Chachitatu ndi CHIYANJANO NDI OKHULUPIRIRA.
(Lembani CHIYANJANO ku mkono wa manja ndi Yohane 13:35.)

Yohane 13:35 akuti, "Mwa ichi adzazindikira onse kuti muli akuphunzira anga, ngati muli nacho chikondano wina ndi mnzake."

Malo enieni oti tikule ndi kukhala mumpingo wa Mulungu. Umo tidzatha kupezana ndi okhulupirira anzathu mchiyanjano cha Chikristu.

- 4) Chachinayi chimene Akhristu ayenera kuchita ndi kuchitira Umboni kudziko lapansi. (Lembani UMBONI kumanzere ndi Yohane 15:8.)

Yohane 15:8 akuti, "Mwa ichi alemekezedwa Atate wanga, kuti mubale chipatso chambiri; ndipo mudzakhala akuphunzira anga."

4. Pamene moyo wanu uyamba kubala zipatso, mungathe kupezana ndi anzanu.

- 1) Kukhala m'Mawu a Mulungu kumatitsogoza ku KUPHUNZITSA.
(Lembani KUPHUNZITSA pansu pa MAWU A MULUNGU.)
- 2) KUPEMPHERA M'CHIKHULUPIRIRO kudzatitsogolera ku KUTAMANDA.
(Lembani KUTAMANDA pamwamba pa mutu.)
- 3) CHIYANJANO NDI OKHULUPIRIRA chimatitsogolera ku KUTHANDIZA mamembala a mumpingo kukula mwa Khristu.
(Lembani KUTHANDIZA pafupi ndi mkono wa manja.)
- 4) KUCHITIRA UMBONI KU DZIKO LA PANSI kumatitsogolera ku ULALIKI.
(Lembani ULALIKI pafupi ndi mkono wa manzere.)